# CHIYAMBI CHA KUPEMBEDZA KWA CHIKHRISTU

## MAYANKHO A MAFUNSO

shepherds
GLOBAL CLASSROOM

# ZAM'KATIMU


1. KUFOTOKOZERA KULAMBIRA 4

2. MULUNGU NDI WOLAMBIRA 6

3. KULAMBIRA MU CHIPANGANO CHAKALE 8

4. KULAMBIRA MU CHIPANGANO CHATSOPANO 10

5. KULAMBIRA MU MBIRI YA MPINGO 12

6. NYIMBO MU KULAMBIRA 14

7. MALEMBA NDI PEMPHERO MU KULAMBIRA 16

8. KUKONZEKERA NDI KUTSOGOLERA KULAMBIRA 18

9. MAFUNSO ENA 20

10. MOYO WA CHIKHALIDWE CHA KULAMBIRA 21

# PHUNZIRO 1

## KUFOTOKOZERA KULAMBIRA

1. Munapatsidwa matanthauzo atatu a kulambira ku mayambiliro a phunziro ili. Lembani tanthauzo limene munaloweza. (Lina lililonse limodzi)

    - Kulambira ndi m'chitidwe wa kulemekeza kochokera kwa munthu kupita kwa Mulungu wa muyaya.
    - Kulambira ndi kukweza mitima yathu mwakufuna kwathu kupita kwa Mulungu.
    - Kulambira ndi kuonetsa chimene ife tili ku zonse zimene Mulungu ali.

2. Lembani maganizo anayi a kulambira. (Zina zilizonse zinayi)

    - Kulambira ndi kugonjera kolemekeza.
    - Kulambira ndi utumiki.
    - Kulambira ndi kuyamika.
    - Kulambira ndi chiyanjano.
    - Kulambira kumakhudza zonse za moyo.

3. Pamene mayi wa ku Samaria anatsutsa za malo opembedzerapo, Yesu anawonetsa **malo a uzimu** opembedzerapo.

4. Mu Masalimo, liwu lakuti **kuyamika** limagwiridwa ntchito pa kunena chimwemwe cha kulambira.

5. Molingana ndi Yakobo, kodi kulambira kumene kuli koona komanso kosadetsedwa kumakhala ndi mbali ziwiri zotani?

    - Kutumikira mwa ntchito.
    - Kumvera kwa tsiku ndi tsiku.

6. Nenani zifukwa zinayi zimene kulambira kuli kofunikira.

    - Mu kulambira timaona Mulungu.
    - Mu kulambira timadziwona tokha ndipo timasinthika.
    - Mu kulambira timaona dziko lathu.
    - Kulephera kulambira kumatilekanitsa ndi Mulungu.

7. Molingana ndi phunziro ili, kodi ndi makhalidwe atatu oti a kulambira amene ali ovomerezeka ndi Mulungu?

    - Kulambira kovomerezeka kumalunjika kwa Mulungu.

- Kulambira komvomerezeka kumapereka ulemelero kwa Mulungu umene amayenera.
- Kulambira kovomerezeka ndi kulambira mu mzimu ndi m'choonadi.

8. Lembani Yohane 4:23-24 kuchokera pakuloweza.

(Onani vesi limene munaloweza pakulinganiza ndi Baibulo).

# PHUNZIRO 2

## MULUNGU NDI WOLAMBIRA

1. Fotokozani zinthu zitatu zimene timaphunzira za Mulungu Mlengi mu nyimbo ya pa Chivumbulutso 4.

    - Mlengi ndi wa Ulamuliro.
    - Mlengi ndi woyera.
    - Mlengi ndi wamuyaya.

2. Tchulani zifukwa zitatu za kulambira Muwomboli mu Chivumbulutso 5.

    - Timalambira Muwomboli chifukwa cha chimene iye ali.
    - Timalambira Muwomboli chifukwa cha kumene iye ali.
    - Timalambira Muwomboli chifukwa cha zimene anachita.

3. Kodi uthenga oyambirira wa Chivumbulutso kwa a Khristu ndi uti?

    Chigonjetso chachikulu cha Mulungu

4. Masalimo 15 ndi Salimo la pemphero logawidwa pa magulu atatu.

    Funso: Kodi ndi ndani amene angalambire?
    Yankho: Kufotokozera wolambira
    Kumaliza kauniuni: Lonjezo kwa wolambira

5. Kodi maganizo a wolambira amene amazindikira kuti ndi mulendo mkupezeka kwa Mulungu ndi otani?

    Kudzichepetsa

6. Kodi ndi makhalidwe ati awiri ofunikira a wolambira owona kuchokera pa Masalimo 15:2-5?

    - Wolambira owona amakhala moyo wa umulungu.
    - Wolambira woona amakhala ndi ubale wabwino ndi anthu.

7. Kodi ndi chifukwa chiyani Yesu anawatcha Afarisi kuti ndi achinyengo?

    - Anthu awa amandilemekeza ine ndi milomo yawo, koma mitima yawo ili kutali ndi ine.
    - Amandilandira ine kwachabe ndi kuphunzitsa malamulo ndi malangizo a anthu.

8. Lembani Chivumbulutso 5:9-14 kuchokera pakuloweza.

(Onani vesi limene munaloweza pakulinganiza ndi Baibulo).

# PHUNZIRO 3

## KULAMBIRA MU CHIPANGANO CHAKALE

1. Kuchokera pa phunziro ili, tchulani zitsanzo ziwiri za kulambira kwa Baibulo kumene kunakanidwa ndi Mulungu. (Zina zilizonse ziwiri)

    - Nsembe ya Kaini
    - Fano la mwana wa ng'ombe wa golide la Aaroni.
    - Moto wachilendo wa Nadabu ndi Abihu
    - Nsembe yofukiza ya Uziya
    - Nsembe yopunduka ya Ayuda ochokera ku ukapolo

2. Mawu akuti *anayendabe ndi Mulungu* akuwonetsa kuti kulambira koona kumakhala **ubale** ndi Mulungu.

3. Kuchokera mu phunziro ili, nenani anthu atatu osayenera amene Mulungu mwachisomo anawapatsa kuthekera kwa kumulambira iye.

    - Adamu ndi Hava
    - Abrahamu
    - Yakobo

4. Nsembe ya Abrahamu ya kupereka Isake ikuonetsa kuti kulambira kowona kumafunika **kumvera** kwa thunthu.

5. Kodi kusiyana kwa kulambira kwa Abele ndi kulambira kwa Kaini ndi kotani?

    - Abele mwakumvera anabweretsa zabwino zake.
    - Kaini anafuna kukwaniritsa ntchito yake mwanjira yosavuta.

6. Kodi kufunikira kwa wolambira kusanjika manja pa mutu pa nyama yoperekedwa nsembe kunali kotani?

    Izi zinafanizira wolambira ndi sembe ya imfa.

7. Mu Buku la Masalimo, muli mitundu iwiri ya kuyamika. Kuyamika kwa chikhalidwe komanso ntchito zamphamvu za Mulungu kumatchedwa **kuyamika** kofotokonzera. Kuyamika kumene kulibe chindunji kumatchedwa **kuyamika** kwa kulengeza.

8. Aneneri akuonetsa kuti **kulengeza** cha uthenga wabwino ndi kulambira.

**9.** Tchulani maganinzo atatu a uthenga wa aneneri pa zakulambira.

- Mwambo wosakhala ndi zenizeni sikulambira.
- Kulambira koona kumafunika kudzipereka kwathu konse.
- Kulambira koona kumafuna moyo wathu onse.

**10.** Tchulani zinthu ziwiri zoopsa zosagwirizana mu kulambira.

- Kulambira mwa chizolowezi
- Kulambira mwa chigulugulu

**11.** Lembani Mika 6:6-8 kuchokera pakuloweza.

(Onani vesi limene munaloweza pakulinganiza ndi Baibulo).

# PHUNZIRO 4

## KULAMBIRA MU CHIPANGANO CHATSOPANO

1. Tchulani njira zitatu zimene Yesu anaperekera zitsanzo za kulambira koona. (Zina zilizonnse zitatu)

    - Yesu anakonda malo wolambirapo.
    - Yesu anakana kulambira wina aliyense kapanena china chilichonse koma Mulungu.
    - Yesu anapemphera mwachikhalidwe.
    - Yesu anafotokozera kulambira koona.
    - Yesu anadzudzula kulambira kwabodza.

2. Kodi kuphunzitsa komanso chitsanzo cha Yesu zikutikumbutsa chiyani za kulambira koona?

    Kulambira koona ndi kwa Mulungu yekha.

3. Kodi ndi ziganizo ziwiri ziti zimene zikufotokozera ubale wa pakati pa kulambira koona ndi kulakira?

    - Kulambira koona kumalimbikitsa kufalitsa uthenga wabwino.
    - Kufalitsa uthenga kwa mphamvu kumapanga wolambira.

4. Kodi kulambira kwabodza kwa Atene kukufotokozeredwa motani pa Machitidwe 17?

    - Anthu a ku Atene anali a chipembedzo.
    - Anthu a ku Atene anapembedza mwa kusadziwa.
    - Anthu a ku Atene analambira Mulungu osaziwika.

5. Kodi Mulungu owona akufotokozeredwa motani pa Machitidwe 17?

    - Mulungu ndi Mlengi.
    - Mulungu ali pafupi.
    - Mulungu adzaweruza amene amakana kulapa.
    - Mulungu anaukitsa Yesu kwa akufa.

6. Tchulani mfundo zisanu za kulambira koyambirira kwa Chikhristu mu mabuku a makalata. (Zina zilizonse zisanu)

    - Kuwerenga mawu
    - Kulalikira Mawu
    - Kupemphera pagulu

- Kuyimba
- Zopereka
- Ubatizo
- Mgonero wa Ambuye

7. Tchulani zitsanzo ziwiri za zotchinga kulambira zopezeka ku mipingo ya ku Ulaya. (Zina zilizonse ziwiri)

    - Kusoweka chikondi
    - Chiphunzitso chabodza
    - Ntchito zakufa
    - Kusoweka kukhudzika

8. Lembani Aroma 12:1-2 kuchokera pakuloweza.

    (Onani vesi limene munaloweza pakulinganiza ndi Baibulo).

# PHUNZIRO 5

## KULAMBIRA MU MBIRI YA MPINGO

1. Tchulani zinthu zitatu za kulambira m'zaka za m'zana loyamba zofotokozeredwa Justin Martyr. (Zina zilizonse zitatu)

    - Kuwerenga kwa Mawu
    - Uthenga
    - Pemphero
    - Mgonero
    - Kupereka mphatso

2. Fotokozerani zifooko zitatu za kulambira mu Zaka za Pakatikati. (Zilizonse zitatu)

    - Kukongola kunali kofunikira kuposa uzimu.
    - Anthu samatha kuzindikira kutumikira.
    - Anthu anali oyang'anira, osati wolambira.
    - Uthenga wabwino unalowedwa m'malo ndi mwambo.

3. Kodi mfundo ziwiri zoyambirira zokhudza Kukozanso unsembe wa okhulupirira ndi ziti?

    - Okhulupirira amalambira Mulungu molunjika.
    - Mawu a Mulungu ayenera akhale opezeka kwa okhulupirira aliyense.

4. Sankhani (ma)gulu mu Kukozanso zimene zikugwirizana ndi kufotokozera kwake.

    - Analola mwambo wina ulionse wa kulambira umene unaletsedwa m'malemba: **Lutheran ndi Anglican**

    - Sanalole mwambo wakulambira umene sunafotokozeredwe m'malemba: **Chiphunzitso cha Calvin**

    - Anakana miyambo yambiri. Nthawi zina analambira mu nyumba zawo: **Chiphunzitso cha Anabaptist ndi a Puritan**

5. Tchulani zinthu zitatu zooneka za kulambira kwa mpingo mwa ufulu.

    - Kulalikira kunali cholinga chachikulu.
    - Kutengapo mbali kwa gulu kunali kofunikira.
    - Mwambo onse wa kulambira unali muchiyankhulo cha anthu.

6. Tchulani zinthu zitatu zimene amakhazikikapo wolambira oyambirira a chi Methodist. (Zina zilizonse zitatu)

    - Ulaliki
    - Mgonero wa pafupipafupi
    - Kuyimba nyimbo
    - Magulu a anthu ochepa
    - Kulambira kwa pamodzi
    - Chisokole

7. Tchulani machitidwe atatu a kulambira mu America m'nthawi zoyambirira. (Zina zilizonse zitatu)

    - Ufulu wa kusakha kukhala mu mpingo wina uli onse komanso machitidwe okhazikika a kulambira
    - Mwayi wapatalipatali wa Mgonero
    - Kulalikira kwa Mawu
    - Kuyimba mwamphamvu
    - Pemphero, chisokole, ndi chitsitsimutso

8. Lembani Masalimo 100:1-5 kuchokera pakuloweza.

    (Onani vesi limene munaloweza pakulinganiza ndi Baibulo).

# PHUNZIRO 6

## NYIMBO MU KULAMBIRA

1. Lembani mndandanda wa nyimbo zitatu zochokera mu Baibulo.

   (Nyimbo zina zlilizonse zimene zanenedwa mu phunziro ili)

2. Kodi ndi zikhulupiriro zotani zimene zinapangitsa Bungwe la Laodekiya kuletsa kuyimba kwa mpingo onse?

   Chikhulupiriro chakuti okhulupirira pawokha alibe kuthekera kapena mwayi wa kumasulira malemba.

3. Tchulani zinthu ziwiri za maphunziro a za Baibulo zimene ziyenera kuonetsedwa mu nyimbo za kulambira.

   - Unsembe wa wokhulupirira
   - Umodzi wa mpingo

4. Tchulani mndandanda wazifukwa zochitika zinayi za nyimbo zolambira.

   - Nyimbo zimayankhula ku maganizo.
   - Nyimbo zimayankhula ku mtima.
   - Nyimbo zimayankhula ku thupi.
   - Nyimbo zimayankhula ku malingaliro.

5. Tchulani mfundo zinayi zimene ziyenera kutsogolera chisankho chathu cha nyimbo. (Zina zilizonse zinayi)

   - Uthenga wa nyimbo za matamando uyenera kupereka choonadi momveka bwino.
   - Maimbidwe a nyimbo za kulambira akhoza kukhala osiyana.
   - Simayimbidwe onse amene ali ogwirizana ndi nyengo iliyonse.
   - Pakhale kugwirizana mu nyimbo zathu za matamando.
   - Nyimbo Zofunika kwambiri za mpingo ndi kuyimba kwa mpingo onse.
   - Nyimbo iyenera kugwirizana ndi uthenga.

6. Kodi ndi mitundu itatu iti ya nyimbo imene yatchulidwa ndi Paulo pa Akolose 3:16?

   - Masalimo
   - Nyimbo zotamanda
   - Nyimbo za uzimu

7. Kodi cholinga chomaliza cha nyimbo zathu za matamando ndi chiyani?

    Ulemelero wa Mulungu

8. Molingana ndi nyimbo za mu Baibulo, ikani mndandanda wa njira zitatu wakuti nyimbo ziyenera kuyankhula ndi magulu osiyansiyana.

    - Nyimbo zikuyenera kulengeza matamando kwa Mulungu.
    - Nyimbo ziyenera zilengeze choonadi ku mpingo.
    - Nyimbo zilalikire za uthenga wabwino ku dziko lapansi.

9. Kodi Akolose 3:16 akuphunzitsa chiyani pa zakufunikira kwa nyimbo za kulambira?

    Tiphunzitsane ndi kulangizana wina ndi mzake ndi nyimbo zathu.

10. Lembani Akolose 3:15-17 kuchokera pakuloweza.

    (Onani vesi limene munaloweza pakulinganiza ndi Baibulo).

# PHUNZIRO 7

## MALEMBA NDI PEMPHERO MU KULAMBIRA

1. Tchulani zitsanzo zitatu zowonetsa kufunikira kwa malemba mu kulambira.

    - Kuwerenga Mawu kunali kofunikira mu kulambira kwa Baibulo.
    - Kulalikira Mawu kunali kofunikira mu kulambira kwa Baibulo.
    - Kulalikira Mawu kunali kofunikira mu Mbiri ya Mpingo.

2. Tchulani mbali zitatu za mwambo wa kulambira pamene malemba akhoza kugwiritsidwa ntchito. (Zina zilizonsse zitatu)

    - Mawu otsegulira mwambo wa mapemphero
    - Kuitanira ku chopereka
    - Mawu a nyimbo
    - Pemphero

3. Tchulani zotsatira zinayi zodziwika za mfundo yakuti *Kulalikira ndi Kulambira.*

    - Kulalikira kumafunika kukonzekera mosamala.
    - Kulalikira kumafunika kuvomereza kuchokera kwa anthu onse.
    - Kulalikira kumafunika kuvomereza kochokera kwa mlaliki.
    - Mlaliki ayenera kupatsidwa mphamvu ndi Mzimu Woyera.

4. Perekani maganizo atatu odziwika a kupanga pemphero kukhala gawo la tanthauzo la kulambira kwa gulu. (Zitatu zina zilizonse)

    - Khazikitsani moyo wanu wa pemphero la mseri.
    - Phunzirani kupemphera.
    - Pempherani mawu a malemba.
    - Khazikikani pa kuyanjana ndi Mulungu
    - Lumikizitsani zofuna zanu ndi za Mulungu.
    - Yankhulani ndi Mulungu, osati mpingo.

5. Tchulani mfundo zinayi za kulambira kwa tanthauzo.

    - Kupereka kokhala ndi kulambira kumalimbikitsidwa ndi chisomo osati mantha.
    - Kupereka kokhala ndi kulambira kumatakasidwa ndi chikondi osati mphoto.
    - Kupereka kwa kulambira ndi kowolowa manja osati kowumira
    - Kupereka kokhala ndi kulambira kumalimbikitsidwa ndi kudzichepetsa osati kunyada.

6. Tchulani mfundo zinayi zodziwika zopangitsa kupereka kukhala m'chitidwe wa kulambira. (Zina zilizonse zinayi)

    - Kutsindika mu chopereka kukhale kulambira, osati zosowa.
    - Chopereka chiyenera kukhala mbali imodzi ya mwambo wa kulambira pachokha.
    - Makolo ayenera aphunzitse ana awo kupereka mu kulambira.
    - Nyimbo mu nthawi ya chopereka ziyenera zikhale za kulambira.
    - Chopereka chitsogozane ndi pemphero la mdalitso.
    - Atsogoleri a mpingo akhale oyang'anira abwino a mphatso za anthu.

7. Tchulani mfundo zitatu za mgonero zovomerezeka mu 1 Akorinto.

    - Tikuyang'ana ku imfa ya Yesu.
    - Tikudikira kubweranso kwa Khristu.

8. Lembani Mateyu 6:5-8 kuchokera pakuloweza.

    (Onani vesi limene munaloweza pakulinganiza ndi Baibulo).

# PHUNZIRO 8

## KUKONZEKERA NDI KUTSOGOLERA KULAMBIRA

**1.** Tchulani zigawo ziwiri zodziwika bwino mu ndondomeko ya kulambira zokhazikika pa uthenga.

- Kulalikira uthenga wa choonadi: kuyimba nyimbo za m'buku, kuwerenga malemba, ulaliki
- Anthu achitapo kanthu kumvomereza choonadi: kuyitanira, chopereka, nyimbo yotsekera mwambo

**2.** Tchulani zigawo zikuluzikulu zinayi mu ndondomeko ya kulambira kutengera pa m'chitidwe wa anthu a Mulungu pa kulambira.

- Anthu a Mulungu asonkhana: Kuyitanira mwambo wa kulambira nyimbo za matamando, pemphero
- Anthu a Mulungu amamvera uthenga: kuwerenga malamba komanso ulaliki
- Anthu a Mulungu achitapo kanthu Kutsatira ulaliki: Nyimbo zam'buku zoyitanira anthu, chopereka
- Anthu a Mulungu atulutsidwa: Nyimbo yam'buku yotsilizira mwambo, Mawu amdalitso

**3.** Tchulani madera atatu mu ndondomeko ya Kulambira yochokera pa Masalimo 95.

- Kulowa ndi chimwemwe cha chiyamiko (Ndime 1-5): kuyitanira pa kulambira, Nyimbo za m'buku zamatamando
- Pitilizani ndi kulambira mwa ulemu: Nyimbo za kudzipatulira kwa Iye, pemphero
- Imvani mau a Mulungu: Malembo ndi ulaliki

**4.** Kodi ndi zinthu zitatu ziti zimene tingakumbukire za kulambira kolinganizika?

- Mwambo wolambira woyanjanitsa mbali zonse umawonetsera Mphamvu ya Mulungu komanso kupezeka kwa Mulungu > pakati pathu.
- Kulambira kolinganiza ndi kwa pagulu komanso kwa aliyense payekha.
- Kulambira kolinganizika kumakhala ndi zodziwika kale komanso zatsopano.

**5.** Mu chitsanzo cha Baibulo cha kulambira, kodi omverera kulambira kwathu ndi ndani?

Mulungu

**6.** Tchulani zoyenereza zitatu za mtsogoleri wolambira wa mphamvu. (Zina zilizonse zitatu)

- Chidziwitso cha uzimu
- Nthumazi

- Mgwirizano
- Chidziwitso
- Nzeru
- Kupirira
- Kudzichepetsa
- Machitachita
- Mwambo
- Kuchita zinthu bwino

7. Kodi ndi zizindikiro zitatu ziti zakuti tikhoza kumasokoneza kulambira? (Zitatu zina zilizonse)

    - Tikamasokoneza maimvaimva ndi kulambira
    - Tikamayelekeza kuti mulingo wa kulambira umafunikira pa kusintha kwa > mtima.
    - Tikamafanizira machitachita a thupi ndi kulambira
    - Tikamafuna kuchita zimene Mulungu anachita nthawi ina kapena > malo ena
    - Tikamayesa utumiki wathu ndi kuthekera kwathu kofuna kupeza chidwi chochokera > kwa anthu

8. Lembani 2 Mbiri 5:13-14 kuchokera pakuloweza.

    (Onani vesi limene munaloweza pakulinganiza ndi Baibulo).

# PHUNZIRO 9

## MAFUNSO ENA

1. Kodi tiyenera kuchita motani ku machitidwe opembedza amene sagwirizana ndi zofuna za chikhalidwe chathu koma satsutsana ndi mfundo za Baibulo?

   Tilore ena alambire munjira imene iwo akufuna.

2. Kodi tiyenera kuchita motani ku machitidwe a kulambira amene ali ololedwa mu chikhalidwe chathu, koma amatsutsana ndi malemba?

   Tiyenera kutsatira Malemba kusiyana ndi ziyembekezo za chikhalidwe chathu.

3. Kodi ndi mafunso atatu otani amene tiyenera kufunsa kuti timvetsetse ubale wa pakati pa kulambira kwa mpingo wathu ndi chikhalidwe chozungulira?

   - Ndi ndani amene ali pano?
   - Ndi ndani amene analipo?
   - Ndi ndani amene akufunika kukhala pano?

4. Kuchokera pa Aroma 14, tchulani mfundo zitatu zogwirizana ndi kulambira.

   - Musaweruze ena za zinthu zokaikitsa.
   - Musakhumudwitse ofooka.
   - Chitani mwa chikhulupiriro, osati mwa kukaikira.

5. Tchulani malingaliro atatu okhudza chipembedzo chopatsira m'badwo wina.

   - Mu malemba, kulambira ndi kopatsirana pa mibadwo.
   - Kulambira kopatsira m'badwo wina kumabweretsa mgwirizano mu Thupi la Khristu.
   - Kudzera mu kulambirakopatsira m'badwo wina, chikhulupiriro chimapatsidwa > ku m`badwo wotsatira.

6. Tchulani zolakwika ziwiri zokhudzana ndi maimvaimva pa chipembedzo.

   - Kukana maimvaimva mu kulambira
   - Kutsindika maimvaimva mu kulambira

7. Lembani Akorinto 14:15-17 kuchokera pakuloweza.

   (Onani vesi limene munaloweza pakulinganiza ndi Baibulo).

# PHUNZIRO 10

## MOYO WA CHIKHALIDWE CHA KULAMBIRA

1. Lembani 1 Akorinto 10:31 kuchokera pakuloweza.

   (Onani vesi limene munaloweza pakulinganiza ndi Baibulo).